



Masewero Oyerekeza Zochitika
Zenizeni
(Role- Play)



International
Labour
Organization

TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro, Zaluso ndi Njira zofalitsira
Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga**

Masewero Oyerekeza Zochitika Zenizeni

Kabukuka ndi kamodzi ka mabuku a maphunziro a TIMVERENI, Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2002 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa angathe kuyikidwa mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa mchitidwe wolembe ntchito ana ipite patsogolo. Ngati mwatanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabukuwa kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI–Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. Kulimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Mchitidwe Ogwiritsa Ntchito Ana pa dziko lonse, International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC), International Labour Organisation (ILO), Geneva, 2002.

ISBN N. 92-2-113 240-4

Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:
International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Organisation (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 77 47
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kuyerekeza zina mwa ntchito zimene ana achichepere ogwira ntchito angachite molumikizana ndi anthu ena (makolo, olemba ntchito, akuluakulu ena amaudindo).



Phindu: Kusonyeza kwa achinyamata mmene angagwiritsire ntchito zitsudzo ngati njira yothandiza kuphunzitsira. Kuyambapo kulingalira zam'mene mavutowa amatikhudzira kudzera m'zisudzo.

Nthawi

Maphunziro awiri olumikizana kudzanso limodzi loonjezera m'zisudzo.



Chidziwitso

Sikoyenera kuyamba gawo lamaphunziro la zisudzo

Chilimbikitso

Zisudzo zimathandiza kuti achinyamata athe kumvetsa bwino lomwe zomwe ogwira ntchito zoposa msinkhu wao angakumane nazo ndiponso mmene angamvere pamoyo wao. Mugawo ili la maphunziro, gulu lonse la ophunzira likupemphedwa kukonza zisudzo malinga ndi zithunzi za ana amene akhala akuwaona pa maphunziro am'mbuyomu. Akuyenera kuyesetsa kukhaladi ngati mwana wokhudzidwayo-monga ngati pankhani yomulekanitsa ndi anthu a m'banja lake, kulephera kupita kusukulu, kukanizidwa kuchita masewera monga momwe zimayenera kukhalira ndi mwana, ululu wa kuchuluka kwa ntchito, kukhala moopsezidwa nthawi zonse, kutopa kodetsa nkhwana ndiponso kusaona tsogolo labwino.

Chidziwitso

Sikoyenera kuyamba gawo lamaphunziro la zisudzo musanayambe kuchita gawo lothandiza kuti ophunzira athe kuyerekeza zinthu zenizeni zochitika m'moyo wa munthu (**Role-play**). Zisudzo zimagawo luso lapadera ndipo zingakhale zovuta kumvetsa kwa amene sanazichitepo m'moyo wao. Choncho zikufunika kuziphunzitsa mwaluso ndiponso mwapang'onopang'ono.

Kuti izi zitheke, choyamba pafunika kuti chinyamata adziwe m'mene angathe kuyerekezera zinthu zochitika m'moyo wa munthu, makamaka kutha kuyerekeza kuona ndi kumva zowawa zomwe kugwiritsa ntchito anazoposa msinkhu wao kungabweretse. Ngati simunachite gawo lothandiza kuyerekeza, chonde yesani kulongosola mwachidule potsindika zinthu monga kuchita kafukufuku ndiponso kufotokoza za komwe nkhani zogwiritsa ntchito ana zawanda kwambiri. Mungathe kugwiritsa ntchito mphindi 15 kapena 20 polongosola gawo la kuyerekezalo mwachidule popeza ndi limene limathandiza ophunzira kuti ayambe kudziwa ndi kumva zamavuto enieni omwe ana ogwira ntchito amakumana nao.

Ngati gawo ili silichitika kukhala kovuta kwambiri kuti ophunzira amvetse bwino nkhani ya zisudzo, ndipo kwa ena zikhala zosatheka kumene.



Sewero loyerekeza zochitika zenizeni (Role-play)

Zisudzo za mtunduwa ndi zimene anthu amayerekeza zimene zimawaonekera ena m'moyo watsiku ndi tsiku. Potambasula pang'ono, tinganenekuti ndi masewero amene anthu otenga mbali amakhala akuchita zenizeni zimene anthu opeka kapena ongoyerekeza amachita. Njirayi ndi yodziwika kwambiri chifukwa imakhala yothandiza munjira zambiri ngati chidachophunzitsira anthu.

Iyi ndi njira yofunitsitsa kuti zonse zimene mwana angamve mumtima mwake ndi kulimbana nazo m'maganizo mwake zituluke poyera panthawi imene maphunziro awa akuchitika. Chofunika kwambiri ndi kutinso zonsezi zithe kukambidwa mozama poganizira mmene zinthu ziliri kwathu kuno pamavutowa.

Cholinga cha **"Role-play"** (masewero a zochitika zeni-zeni) kapena kuyerekeza musewero zimene zimachitika ndikufuna kuti achinyamata athe kumvetsa bwino kwambiri za mavuto enieni ndikuwalingalira mozama. Poyerekeza mavuto osiyanasiyana okhudza kugwiritsa ntchito ana zoposa msinkhu wao, achinyamata akuyembekezeka mwanjira ina kulowa m'moyo wa ana okhudzidwawo ndi kutha kuwamvetsa, kumva m'mene angamvere mumtima mwao. Zonsezi akuyenera kuzionetsa mu **Role-play**. Njira iyi yophunzirira ndi yothandiza kwambiri ndipo ikuyenera kubweretsa kusintha ndi zotsatira zina zabwino m'moyo wa achinyamata.

Kupatulapo Masewero a Zisudzo (**Drama**), zisudzo za mtundu uwu ndi zothandiza kwambiri kuti achinyamata amvetse bwino lomwe za kugwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu ndi zipsyinjo zonse zimene zingathe kupezeka m'moyo wao. Poonjezera apo, njirayi imapereka mphamvu ndi mangolomera kwa ophunzira. Chimene chimachitika ndichakuti pamene atsiriza gawo limodzi lamaphunziro ndipo akulowa mugawo lina, amakhala akutenga umwini wa vutoli. Tili ndi chikhulupiliro kuti pandime ino ayamba kuzindikira kuti kugwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu ndi vuto lomwe limakhudza aliyense padziko lino lapansi, ndipo motero munthu aliyense ayenera kutengapo gawo ndi udindo wake kuti mchitidzewu uthetsedwe.

Ndiponso poonjezera apo, iwo ayenera kuyamba kumvetsa kuti role-play ndi njira yamphamvu yoperekera uthenga kwa anthu.

Kukonzekera



Nthawi zambiri zimakhala zovuta kupeza kuti ena kapena onse mwa ophunzira anu akumvetsa kale za zisudzo. Choncho, inu mukuyenera kuchita zonse zotheka kuyambira pachiyambi kuti achinyamata apeze phindu lalikulu ndi zonse zochitika zokonzekera gawo ili la zisudzo pofuna kuti zizolowezi, maganizo ndi khalidwe lao zithandize pantchitoyi. Zitsanzo zina za zochitachita zogwirizana ndi role-play zilipo kotsiriza kwa buku lino. Inu mungathe uwonjezerapo zina kudzera mukafukufuku wanu. Komanso pali zina zambiri zomwe zingathandize pantchitoyi zomwe zingapezeke mgwirizano wa makompyutala wofalitsira mauthenga (**internet**) ndiponso mabuku ena onlongosola za zisudzo.

Chidziwitso

Gawo ili lamaphunziro lingathe kutenga nthawi yochuluka kwambiri. Mwachitsanzo njira yoimitsa role-play ndi kuyamba kupereka maganizo pofuna kutsindika mfundo payokha ingathe kutenga ola limodzipotengera ndi kuchuluka kwa anthu amene akutenga mbali ndiponso nthawi yomwe angasowe kuti akonzekere. Masewero a zisudzowonso angathe kutenga nthawi yaitali. Choncho muyenera kukonza dongosolo lanu mosamala kwambiri kuti muimitse zisudzozo panthawi zofunika kwambiri zokhazokha kuti anthu akambirane mozama. Mwachitsanzo, paphunziro lina mungathe kungochita zokonzekera zokha ndipo paphunziro lina kuona mozama mfundo zomwe zikuperekedwa ndi kuzikambirana.



Zingakhale zothandiza kwambiri kwa inu kuti pamaphunziro awa mufufuze ndi kupeza akatswiri oti akuthandizeni. Sibwino kuti mudzikhulupilire nokha kwambiri pagawo ili, koma zingakuthandizeni kupeza kadaulo weniweni woti akuthandizeni ndi luso lenileni lovomerezeka. **Role-play** ndi yothandiza pamene mukuyamba kulongosola za masewero a zisudzo kwa achinyamata mwina chifukwa zimathandiza kwambiri kusinkhasinkha aliyense payekha. Komanso mwina chifukwa choti achinyamata amakonda kuchita zinthu mongotengera amnzao. Penanso luso limene lagwiritsidwa ntchito pochita **role-play** limamupatsa munthu chithunzi chofunika kwambiri cha mmene mavuto aliri. Ingathe kukhala ntchito yovuta ndithu kuti achinyamata ayambe kumasuka ndi kuchita role-play, koma katswiri weniweni, mkhalakale kapena mphunzitsi pa masewerowa angathe kukuthandizani kuti zinthu ziyambe kuyenda monga mukufunira.

Kupeza chithandizo

Choti mudziwe ndi chakuti simuyenera kuchita kuswa mutu pofuna munthu wotere kuti mwinanso zingafune ndalama zambiri. Ngati sangapezeke pafupi musadandaulekwambiri. Mwinanso khola la mmodzi mwa achinyamatawo ingathe kukuthandizani. Komanso ndi kofunika kumva maganizo ndi nzeru zina kuchokera ku gulu lanu.

Zofunikira



Zofunika mugawo ili ndi zochepa kwambiri. **Role-play** imangofuna kuunika bwino zochita za amene akutenga mbaliwo. Zina ndi zina zokhala pamalo ochitira role-play zimakhala ngati zongoonjezera komanso zingathe kukhala zosokoneza kwa oonera ndi ochita **role-play**. Gulu liyenera kuonanso bwino kuti ndi chiyani chimene chikuphezeka pamalopo chimene angathe kugwiritsa ntchito.

Choncho, ngati pali matebulo, mipando ndi katundu wina m'chipindamo, izi zingathe kugwiritsidwa ntchito ngati kuli kofunika kutero. Ndi chinthu chofunika kukhala m'chipinda chimodzi momwe mukuchitira zonsezi. Ngati gulu lili lalikulu kwambiri, ndi bwino kuligawa m'timagulu tocheperako kuti kagulu kalikonse kakhale m'chipinda chake ngati izi ndi zotheka.

Ndikofunika kwambiri kuti inu muthe kutsata bwino zonse zimene akuchita powayendera m'timagulu tawoto ndi kuwalimbikitsa komanso kuwapatsa malangizo oyenera.

Kuyamba



Tengani mphindi zokwana khumi koyamba kwa phunziro anu loyamba mugawo lino. Choyenera kuchita ndi kuunika bwino zokhudza ana ogwiritsidwa ntchito omwe munawapeza mugawo loyamba loyerekeza zinthu. Thandizani gulu kuti limvetse bwino za ana amene iwo anapatsidwa kapena kusankha kuti awatsatire bwino mbiri zao.

Gulu: Muyese kudzala umwini weniweni komanso udindo m'gululo. Magulu onse achite chimodzimodzi. Ndikofunika kuti onse akhale chete pamene inu mukuzungulira kuyesa kuthandiza magulu osiyanasiyana powalankhula ndi kuwapatsa chidwi choti athe kuchitapo kanthu. Athandizeni kukonzanso zithunzi zosiyanasiyana m'maganizo mwao.

Kukonza magulu

Yesetsani kuti gulu lililonse likhale chimodzimodzi mmene anakhalira pamene mumachita gawo loyerekeza zithunzi zosiyanasiyana. Akuyenera kuti pofika nthawiyo akhale atazolowerana ndipo izi ndi zimene zingakuthandizeni kuti zinthu ziyende bwino.

Pofuna kuti zikhale zopindula kwambiri, magulu akhale ndi achinyamata okwana anayi kapena asanu koma osapitirira apo. Magulu akakula, ena amalephera kuonetsa luso lawo pobisala m'chigulu. Nthawi zambiri achinyamata akapeza mwayi wozemba ntchito ngati izi, sakaika kutero. Kuchepetsa kuchuluka kwa anthu m'gulu lililonse kumathandiza kuti iwo aone chovuta kubisala mwamtunduwu.



Kumbukiraninso kuti kusakaniza anyamata ndi atsikana kumathandiza kukometsa zinthu muzisudzo zamtunduwu.

Gawo loyamba la zochita: Zochitachita pokonzekera sewero

Phunziro limodzi

Ndikofunika kuti pakhale maphunziro okhudza zisudzo zochitika zonse zokhudza masewero zisanayambe. Komabe zingathe kutheka kuyamba kuphunzitsa izi zisanachitike ngakhale kuti izi zingakhoze kupangitsa kuti ophunzira asamvetse zina ndi zina zofunika. Kothera kwa gawo lino la maphunziro kuli mitundu ya masewero yosiyanasiyana komanso pali ina imene ikupezeka m'dera mwanu imene ili yogwirizana ndi chikhalidwe chanu.

Njira ina yomwe zisudzo zingaphunzitsidwire ndi kudzera m'masewero monga ongogwiritsa ntchito zizindikiro osalankhula, ndipo tanthauzo lake laperekedwa komalizira kwa gawolino la maphunziro (**charades**).

Cholinga chachikulu ndi kupangitsa achinyamata kuti athe kuika maganizo ao kuti athe kukhala omasuka bwino, osachita manyazi ndinso kuti asamaganizire kwambiri za zimene iwo akuchita, komanso mmene ena akuchitira kapena zokamba zao pamene akuonera zisudzo zimene iwo akuchita. Izi ndi zimene zingathandize kuti iwo athe kukhala odzikhulupilira.

Gawo Lachiwiri La Zochita: Kuyimitsa Sewero Mwa Dzidzidzi ndi Kuchita Ndemanga

Phunziro limodzi



Chidziwitso

Zisudzo zogwiritsa ntchito zigawo zosiyanasiyana zazifupi zam'masewero zomwe zimaimitsidwa ndi kutambasulidwa ("**Freeze-frames**") ndi njira yabwino yoyambira kuphunzitsa za zisudzo.

Koma izi ndi zofuna nthawi yambiri ngakhale magulu akhale ochepa. Choncho ngati nthawi ilipo yokwanira, ndi kwabwino kugwiritsa ntchito njira imeneyi zisudzo zenizeni zotalikirapo zisanayambe. Koma ngati nthawi yanu ndi yosakwanira, njira iyi mungathe kuidumpha kuti musataye chidwi cha ophunzira. Chinthu choyamba chimene amachita ndi kuchotsa manyazi omwe nthawi zina amatenga nthawi yaitali asanakhale akaswiri a zisudzo.

Mosakaika mupeza achinyamata ena pakati pagulu limene mukuliphunzitsa omwe akuonetsa kuti ali ndi luso. Ichi ndi chinthu chosangalatsa kwa inu popeza muona kuti mwatsegula tsogolo loyenera. Apa chidwi, luso ndi mphamvu zao zingangiritsidwe ntchito moyenera. Alimbikitseni ndi kupititsa patsogolo kudzikhulupilira kwao chifukwa uku ndiye kupita patsogolo kwa moyo wao.

Poganizira nthawi yomwe muli nayo, gulu lisanayambe kuphunzira za masewero oyerekeza zochitika m'moyo wa munthu, njira yabwino yoyambira ndi kuchita zisudzo zimene osewera amaimitsa pakati ndi cholinga chofuna kukambirana ndi kutsindika mfundo zina zofunika.

Gulu lilonse lipatsidwe mitu iwiri kapena itatu ndipo ayese kupanga kasewero kakafupi komwe zochitika zake zingaonetsedwe kudzera muzimene munthu akuonetsa ndi thupi kapena gawo la thupi lake. Pakhale mutu umodzi waukulu (monga mwambo wa ukwati kapena maliro, kapena china chilichonse chochitika m'moyo wa munthu kapenanso zochitika mosayembekezeka) ndiponso mutu wina wokhudzana ndi kugwiritsa ntchito ana ochepa nsinkhu.

Njira iyi ndi yofanana pang'ono ndi imene ilinso m'maphunziro ano momwe aliyense wochita nawo zisudzozi amakhala ngati kachithunzi komwe kang'ambidwa m'magazini ndi kuikidwa pamodzi ndi cholinga chofuna kulongosola mutu wa nkhani ina imene yasankhidwa.

Sankhani mitu imene magulu onse akuidziwa bwino, lolani kuti maganizo osiyanasiyana aperekedwe ndipo anthu akambirane momasuka pamitu yonse. Onesetsani kuti mitu imene angasankheyo ikhale yogwirizana ndi zolinga za maphunzirowa kuti iwo athe kutenga mbali bwino.

Poganizira nthawi yomwe muli nayo, gulu lisanayambe kuphunzira za masewero oyerekeza zochitika m'moyo wa munthu, njira yabwino yoyambira ndi kuchita zisudzo zimene osewera amaimitsa pakati ndi cholinga chofuna kukambirana ndi kutsindika mfundo zina zofunika.



Gulu lilonse lipatsidwe mitu iwiri kapena itatu ndipo ayese kupanga kasewero kakafupi komwe zochitika zake zingaonetsedwe kudzera mu zimene munthu akuonetsa ndi thupi kapena gawo la thupi lake. Pakhale mutu umodzi waukulu (monga mwambo wa ukwati kapena maliro, kapena china chilichonse chochitika m'moyo wa munthu kapenanso zochitika mosayembekezeka) ndiponso mutu wina wokhudzana ndi kugwiritsa ntchito ana ochepa msinkhu.

Njira iyi ndi yofanana pang'ono ndi imene ilinso m'maphunziro ano momwe aliyense wochita nawo zisudzozi amakhala ngati kachithunzi komwe kang'ambidwa m'magazini ndi kuikidwa pamodzi ndi cholinga chofuna kulongosola mutu wa nkhani ina imene yasankhidwa.

Sankhani mitu imene magulu onse akuidziwa bwino, lolani kuti maganizo osiyanasiyana aperekedwe ndipo anthu akambirane momasuka pamitu yonse. Onesetsani kuti mitu imene angasankheyo ikhale yogwirizana ndi zolinga za maphunzirowa kuti iwo athe kutenga mbali bwino.



Yesetsani kuti aliyense atenge mbali. Ina mwa mitu ingathe kukhala zimene zimachitika pamene ana ochepa misinkhu agwiritsidwa ntchito kapena kuzunzidwa munjira zina. Zitsanzo zingathe kuchokera ku malo ngati ntchito za ulimi, kapena malo amene muli makina omwe angathe kupereka chiopsezo kumoyo wa ana, mchitidwe wachiwerewere kapenanso kuzunzidwa kwa m'banja.

Zisudzo Zoyerekeza Zochitika M'moyo

- 1) Yesani kuona mitu imene siikunyoza kapena kukhumudwitsa magulu ena a anthu
- 2) Yang'anani nkhani, nthano ndi zithunzi zimene iwo akhala akuziona ndi kukambirana ndikupeza mitu yomwe pangachokere sewero.
- 3) Ganizirani zosowa za gulu lanu ndi zimene iwo akomana nazo m'moyo wao ngati mukuwadziwa.
- 4) Kugwiritsa ntchito luso la zisudzo kumathandiza kuti anthu amve mumtima mwao zenizeni zimene zikuonetsedwa musewero ndinso kufuna kuchitapo kanthu. Ndikutheka kuti ena mwa achinyamata m'gulu lanu anakomana ndi mavuto ozunzidwa mwamtundu uwu. Ena mwina anazunzidwa ndipo pochita zisudzozi akhala okhudzidwa kwambiri pokumbukira mavuto ao. Ndipo ena wina anagwiritsidwa kapena adakagwira ntchito zoika moyo wao pachipsezo. Mukuyenera kuona bwino zamtunduwu pokonzekera ndikuona mmene mungathanirane ndi mavuto onse obwera chifukwa cha izi.
- 5) Mukapez zosiyanasiyana za zisudzo zanu, kambiranani ndi gulu lonse mmene mungachitire masewero othandiza kupereka bwino mauthenga oyenera.
- 6) Onesetsani kuti iwo akumvetsa bwino zoyenera kuchita.
- 7) Pamene mwaona kuti iwo ndi okonzeka kuchita masewero awo, agaweni m'timagulu tawo ndi kuwapatsa mphindi khumi kuti akonzekere timasewero tawo.

Poyendera maguluwa alimbikitseni ndi kuwathandiza. Ngati pali katswiri amene mwamuitana kuti athandize pantchitoyi, onesetsani kuti azungulire ndi kuthandiza magulu onse moyenera.

- 1) Onesetsani kuti zonse zimene akufuna kuonetsa ndi zogwirizana ndi mitu imene anapatsidwa ndipo ngati kuli kofunika athandizeni kukonza zolakwika.
- 2) Mukaona kuti zonse zakonzeka, bweretsani magulu onse pamodzi kuti ayambe kuonetsa zisudzo zawo.

- 3) Gulu lililonse likamaliza kuonetsa zisudzo zake, onesetsani kuti gululo likukambirana pa zimene laonetsa motsogozedwa ndi mafunso ngati awa: *Kodi gululo linamvetsa bwino nkhani yonse? Ndi pati pamene pamafunika kukonza? Kodi gululo linachita zonse zotheka pazisudzo zake?*
- 4) Yesani kuyambitsa zokambirana mozama pounikira zimene gulu lililonse lachita ndi kuonetsa.
- 5) Onesetsani kuti zisudzo zikutsatirana mofulumira china chikatha poopa kutaya nthawi yambiri.
- 6) Yesani kuchititsa kuti zikhale zosangalatsa poonetsetsa kuti pali kupikisana, ndipo ngati kungatheke, pakhale mphotho kwa ochita bwino koposa onse.
- 7) Amene angaweruze kuti zikuyenda bwanji angathe kukhala magulu omwewo. Ngati pali woonelera wapadera, monga katswiri wa zisudzo, mupempheni kuti azichitira ndemanga pa momwe zisudzozo zikuyendera. 8) Ngat nthawi ilipo, wonjezerani zina zimene mungaone kuti zikusowa muzisudzozo. Komanso china chofunika kuchiona bwino ndi chidwi cha achinyamata muzisudzo.
- 9) Pemphani magulu onse kuti asankhe mutu wa zisudzo zawo ndipo asaulule kwa magulu ena.
- 10) Magulu apatsidwe mphindi zisanuzoti akonzekere.
- 11) Uzani magulu onse kuti aonetse zomwe akonza ndipo yesani kupeza zisudzo zimene ena angathe kuzitanthauzira msanga kuposa zinzake. Zochitika izi ndi zothandiza kuti achinyamata ayambe kumvetsa zochitika muzisudzo kuti pamakhala zina zoonekeratu poyera ndipo zina zosinjilira. Zisudzo zosalankhula zikuyenera kukhala zoti ena onse athe kuzimvetsa.

Choncho, mungathe kugwiritsa ntchito zisudzo zosalankhula kapenanso zoimitsa pakati pophunzitsira mmene zinthu zimakhallira m'masewero. Zina mwa izo ndi ngati kusatchingirana, kapenanso kusonyeza msana kwa oonera.

Gawo lachitatu la zochita: Role-play

Phunziro limodzi

Konzani magulu monga munachitira muphunziro la m'mbuyomu. Apatseni mphindi makumi awiri (20) kuti ayambe kukonzeka. Nthawi ikatalika kwambiri chidwi cha ophunzira chimachoka.

Iwo akonze sewero limene likuonetsa kugwiritsa ntchito ana ochepa msinkhu limene chithunzi chake anapanga kale mu gawo la m'mbuyomu.

Iwo akuyembekezeka kuonetsa ena mwa mavuto omwe mwana angagwemo pamene akugwira ntchito yomwe ndi yobweretsa chiopsezo m'moyo wake. Zina zoyembekeza kuoneka ndi ululu woona kuti tsogolo lake silikudziwika bwino ndiponso kusowa kwa zinthu zosiyanasiyana zothandiza kuti moyo wake ukhale watanthauzo.

Zingakhalenso bwino kuti poonetsa zisudzozo, anthu ena omwe iye angathe kukumana nawo m'moyo wake watsiku ndi tsiku athe kupezekamo. Zitsanzo ndi olemba ntchito, makolo, ogwira ntchito ena, achitetezo ngati apolisi, anthu omwe akuchita nawo malonda (monga zimakhallira pa nkhani ya uhule) ndi ena otero. Uwu ndi mwayi wabwino wobweretsa mbwalo nkhani ina yokhudza kulimbikitsa kupereka mwayi wofanana kwa amuna ndi akazi (**gender**) mokhudzana ndi mchitidwe umenewu wogwiritsa ntchito ana.

Mwachitsanzo, ngati mwana amene ali musewero ndi wamkazi, funso limene lingakhalepo monga kumbali yamaphunziro ndi loti kodi mwayi wake wamaphunziro ndi wotani poganizira mtundu wa ntchito yomwe akugwira?

Poganizira chikhalidwe ndi mavuto a m'dera lanu, mungathe kukambapo za kuchitira ana aakazi chipongwe kumbali yogona nawo. Mavuto ngati omwewa angathenso kukhudza ana amuna. Onesetsani kuti gulu liganizire mavuto awa ndi kuwaika m'zisudzo zawo.

Zisudzozo zikuyenera kuonetsa nthawi zomwe ana olembedwa ntchito angakumane ndi zokoma kapenanso zokhoma. Zina mwa zinthu zimene magulu onse akuyenera kumvetsa pokonzekera zisudzo za mtunduwu ndi izi:

- zisudzozi akuzichita pamaso pa anthu ena amene akuonera;
- akuyenera kulankhula mokweza, momveka bwino ndipo mwapang'onopang'ono kuti mau onse amveke bwino;
- akuyenera kuganizira mwambo wazisudzo monga ngati osatchera misana kwa anthu oonera;
- asayendeyende kapena kudzigwedeza mopyola muyezo; ayesetse kufanizira bwino lomwe zimene anthu amene akuwafanizira amachita ndikuyesetsa kuonetsa luso lawo lonse;
- aliyense atenge nawo mbali.

Magulu omwe angafune kuti achite kulemba sewero lawo ayesetse kupanga zinthu zathanthauzo, kuti koyamba ndi kothera kwake kumveke bwino ngakhale kuti kusiya anthu m'malere kothera kumakhala kwabwino nthawi zina. Ena amanena kuti kuchita kulemba zoti alankhule muzisudzo kumapangitsa ena kuti asaonetse luso lawo lonse. Motero, inu mungathe kutsata njira iliyonse imene mungaone kuti ndi yabwino.



Kukonzekera



Magulu akagawidwa, inu muyambe kuzungulira kuti muone mmene zinthu zikuyendera.

Ngati mwaitana katswiri wa zisudzo woti akuthandizeni, mupempheni kuti iye agwire ntchitoyi.

Khalani ndi gulu lililonse ndi kuonesetsa kuti lithe kuona zinthu zochitikadi ndi kuziika musewero. Panthawi iyi iwo asadzikhulupilire kwambiri.

Athandizeni kupeza mutu ndipo pamodzi muone mmene mungautambasulire. Adzifunse kuti kodi akufuna kuonetsa zokoma kapena zokhoma/zowawa? Poyamba penipeni adzifunse kuti kodi chenicheni chimene iwo akufuna kuonetsa anthu chiyani?

Athandizeni kugawana maudindo kapena zochita, kapenanso ngati akufuna kuchita zolemba, athandizeni kutero. Iwo asakhutitsidwe kwambiri panthawi imene akungolembe sewero lawo.

Aganizire m'mene anthu osiyanasiyana musewero angamvere pamene iwo akuchita zisudzozo ndi zimene iwo angamachite. Kodi adziseka? Kapena kuomba m'manja? Kodi adzimva chisoni kwambiri ndi kumakhetsa misozi?

Aone bwino lomwe kuti ndi ndani amene angathe kutenga udindo wopereka uthenga waukulu wazisudzo zanu. Ndipo amene angatenge mbali ya mwana ndi woyeneradi? Athandizeni kumvetsa bwino ndi kulongosola bwino za makhalidwe a anthu omwe akuwafanizira muzisudzo komanso kuona kuti adzigwiritsa bwanji matupi awo.

Limbikitsani onse amene ali m'magulu chifukwa ena azikhalabe ndi manyazi. Auzeni kuti aziyerekeza ngati palibe amene akuonera. Nthawi zambiri achinyamata amakhala ndi vuto loopa kusekedwa ndi kupatsidwa maina. Akangochotsa vuto ili zina zonse zimayenda bwino.

Adziwebe kuti pamene akukonzekera pazikhala phwete ndi kusekana apo ndi apo. Chofunika ndi choti wina aliyense asakhumudwitsidwe ndi ndemanga kapenanso kutonzedwa mopitiriza muyezo.

Onani m'mene zinthu zikuyendera pamene mukuzungulira m'magulu. Lumanani khutu ndi katswiri amene mwamuitana kuti akuthandizeni ndikuona ngati yafika nthawi yoti ophunzira angathe kuonetsa zisudzo zawo kwa ena.

Kutalika kwa nthawi yoyesera zisudzo kungatengere mmene iwo angasowere upangiri komanso mmene iwo akumvera m'magulumo chifukwa zimakhala zotopetsa.

Ngati munaphatikiza zisudzo zosalankhula kapena zoimitsa pakati mu phunziro limodzi ndi masewero awa, ndi chachidziwikire kuti panthawiyi magulu angakhale atayamba kudandaula ndi kuonetsa zizindikiro zotopa.

Kuwonetsa Sewero

Zonsezi ndi zolemetsa ndipo zili kwa inu kuona pamene magulu akusonyeza kutopa komanso mmene zonse zikuyendera. Ngati zingatheke kukonzekera ndi kuonetsa zisudzozo mu mlingo umodzi wa maphunziro, zingathe kukhala zabwino ndithu. Koma pamene muona kuti iwo afika potopa, mungathe kuimira pazokonzekera pomwepo kwa nthawi imeneyo ndipo kuonetsa zisudzozo kwa magulu ena kungathe kudzachitika nthawi ina.

Pazonse zimene mungachite, onetsetsani kuti zokonzekera zachitika ndipo kuti aliyense akuoneka wokhutitsidwa ndi gawo limene wapatsidwa.

Magulu onse akakonzeka, asonkhanitseni pamodzi

Yalani mipando mbali imodzi ya chipinda chimene mwasonkhana Konzani bwalo lomwe magulu adzionetsera zisudzo mbali ina ya chipindacho .

Konzani m'ndandanda wa mmene magulu aonetsera zisudzo zawo mogwirizana

Magulu ambiri amakonda kuti akhale koyamba kuti "angothana nazo"

Ulutsani m'ndandanda wonse kwa magulu onse

Onesetsani kuti pali mwambo ndi dongosolo labwino pamene magulu akuonetsa zisudzo zawo

Yesetsani kuti gulu lililonse lipatse ulemu ndi magulu ena pomvetsera mwakachetechede

Mukulangizidwa kulemba zimene mukuona kuti ndi zofunika kukambirana pamene gulu lililonse likuonetsa ndipo izi zikuthandizani panthawi yokambirana



Chidziwitso

Muyesetse kuti ndemanga zanu pa zisudzo zosiyanasiyana zisakhale zokhumudwitsa kapena zoononga.

Musaonetse kuyamikira kwambiri munthu mmodzi kapena anthu ochepa Gulu lililonse likamaliza, mutsogolere kuomba mmanja ndi kuyamikira zimene iwo aonetsa ndi kuchita ndemanga zowalimbikitsa ndipo mukatero muona kuti gulu lonse lichita chimodzimodzi ngakhale atachoka pabwalo lochitira zisudzo Izi zithandiza kuti aliyense amve kuti zimene wachita ndi zopambana ndipo kuti angathe kuchita zoposa apo

14 TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana



- Gulu lililonse likamaliza kuonetsa zisudzo zake, perekani mpata kwa magulu onse kuti achite ndemanga ngakhale kuti pomaliza penipeni pakuyenerakukhala mwayi wokambirana mozama mmene zinthu zayendera
- Chofunika kwambiri ndi kuti magulu onse akhale ndi chidwi chophunzira kuchokera kwa amnzawo.
- Mungathe kutsatira mfundo izi:
 1. Perekani ndemanga yachidule pa m'mene nkhani yonse inakonzedwera, komanso chilichonse chimene aona ndi kumva
 2. Pangakhale zinthu zina zimene zikanachitidwa bwinoko kapena mwanjira ina pa zimene mwaona ndi kumva?
 3. Mukuti bwanji pa luso limene wina aliyense waonetsa pazisudzo zimene mwaonera pano? Muyesetse kuti mulole mfundo zolimbikitsana zokha.
 4. Nanga mauthenga amveka bwanji poganizira kuti aliyense anali ndi mbali yake yochita?
- Mukuyenera kulimbikitsa mtima wochita zinthu mopita patsogolo komanso kulimbikitsa umwini ndi udindo wa mauthenga pakati pa achinyamata poonesetsa kuti onse akuchita zinthu mothandizana ngati amodzi. Izi zimapititsa patsogolo mtima wodzidalira
- Ngati munaitana kadaulo wa zisudzo kuti akuthandizeni, ndemanga ndi mfundo zimene angapereke ndi zofunika kwambiri kuti achinyamata azigwiritse
- Poonelera ndi kumvera mukuyenera kulemba mfundo zonse ndi kuona luso lapadera lililonse la zisudzo limene aliyense angakhale nalo. Mukuyenera kuchita chimodzimodzi poyesa kuona luso loyala bwino ndi kulemba zisudzo. Zonsezi zifunika kuti muzigwiritse ntchito m'maphunziro ena a zisudzo.
- Sibwino kukonza zinthu ngati mpikisano panthawi iyi chifukwa kufanizira zochitika ndi chinthu chimene chimafunika kuti munthu adzipereke kwathunthu ndipo achinyamata amavutika kuti aphimbe makhalidwe awo enieni ndipo pamene mwawafanizira ndi ena zimatha kuwakhumudwitsa.
- Yesetsani kuti iwo aone kuti zonse zayenda bwino.

Zoyenera kuchita ndi zoyenera kupewa



- Onetsetsani kuti onse akuchita zinthu mwamtima umodzi ndipo izi zingathandize kuti zisudzo zonse ziyende bwino.

- Pamene mukukhudza zinthu zokhudza kupereka mwayi wofanana kwa amuna ndi akazi, mukuyenera kusamala kwambiri. Nkhani zogonana zimaika pachiposezo moyo wathupi komanso wam'maganizo ndipo mfundo izi zikuyenera kukhudzidwa pamene tikukamba za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ochepa msinkhu. Komabe pena pake ndi kovuta kukamba mozama mavuto onse ndipo anthu onse ophunzitsa ayenera kudziwa kuti nkhani zake zimakhala zovuta kwambiri (choncho mphunzitsi aganizire msinkhu wa ana omwe akukamba nawo nkhani ngati zimenezi).

- Yesetsani kuti aliyense atenge mbali pofuna kuthetsa manyazi ndi makhalidwe ena amene amalepheretsa achinyamata kuchita zinthu momasuka.

- Onesetsani kuti chidwi chimene chilipo chikhalepobe mpaka pothera pa zonse chifukwa chikachoka pangathe kukhala zambiri zosokoneza zimene achinyamata angafune kumachita.

- Yesetsani kuti zomwe magulu akulankhulana mocheza zikhale zosangalatsa ndipo zosanyozana. Cholinga chake chikhale kulimbikitsana osati kukhumudwitsana.

- Musalole kudzudzulana kapena kugwiritsa ntchito mau onyozetsana panthawi yonse yamaphunzirowa. Izi zingagawe gulu ndipo mtima woti akuchita zinthu limodzi ungachoke. Sizifunika kuti mtima wa mpikisano ulamulire pa zisudzo zamtundu uwu chifukwa luso lina silingatuluke bwino.



- Ngati pali gulu lina loti likuvutika kwambiri, lithandizeni ndi luso lanu lonse. Mungathe kulowelera ndi kutenga nawo mbali pamene mwaona kuti kukufunika kutero. Ngati pali ena ofuna kusiyira panjira, aloleni kutero

- Ngati mulindi chida chojambulira (**video camera**), chigwiritseni ntchito chifukwa chimathandiza pokambirana zimene zinachitika. Komanso achinyamata angasangalale atadziona okha pa kanema.

- Nthawi yokambirana ikafina, perekani mwayi wokwanira kwa achinyamata kuti athe kulankhula za kukhosi momasuka. Aloleni kuti adziseke okha ndipo izi ndi zothandiza kuti zimene aphunzira zikhale zosaiwalika.

Kukambirana komaliza

Phunziro limodzi

- Nthawi yokambiranayi ndi yofunika kwambiri ndipo ikuyenerakuchitika pamene gulu lililonse lamaliza kuonetsa zisudzo zake.
- Uzani aliyense kuti akhale pansu ndipo tengani zonse zimene mwalemba pokonzekera zokambiranazo.
- Ngati pali kadaulo wa zisudzo amene munamuitana, nayenso akhale wokonzeka kulankhula ndi kupereka ulangizi wake.
- Limbikitsani gulu lonse kukamba momasuka pa zimene anaonetsa ndinso mmene iwo anamvera
- Apempheni kulongosola momveka bwino momwe iwo eni anamvera. Mungathe kugwiritsa ntchito mfundo ngati izi:
 1. *Kodi munamva bwanji pamene mumachita zisudzo pamaso pa amnzanu?*
 2. *Nanga munalibe mantha, kapena zinjenje?*
 3. *Kapena munaliosangalala kwambiri? Nanga chimene chinapangitsa izi ndi chiyani?*
 4. *Nanga munaona kuti uthenga umene mumapereka ndi wofunika bwanji? Nanga unakukhudzani bwanji?*
 5. *Kodi zisudzozi zakuthandizani kumvetsa bwino za mavuto amene mwana yemwe amagwiritsidwa ntchito yoposa msinkhu wake amamvera?*
 6. *Nanga zimene mwachita ndi zokupangitsani kuti mufune njira zothandizira mwana wotero?*
- Pangani zotheke kuti achinyamata a m'magulu ena apereke ndemanga zothandiza kukonza zinthu, athe kufunsa mafunso ndi kutambasula zimene ndemanga zawo zokhudza zimene iwo aona. Ngati munajambula pa kanema, iyi ndinthawi yoti muionetse pang'onopang'ono ndi kumaimitsa popereka mwayi woti achinyamata athe kupereka maganizo ndi ndemanga zawo. Ena amakhala okondwa kwambiri podziona okha pakanema. Uwunso ukhala mwayi woti athe kulandira upangiri wa m'mene iwo angachitire zisudzo.
-
- Mothandizana ndi katswiri amene mwamugwiritsa ntchito, mungathe kuona ndi kutambasula mfundo zina zothandiza kutukula luso la zisudzo. Pofuna kuthana ndi mchitidwewogwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu, chofunika kwambiri ndi kusintha kaganizidwe komanso makhalidwe ena a anthu. Izi zimachitika kudzera m'maphunziro ndipo achinyamata ali ndi udindo waukulu pothandiza kudzisula okha ngati othandiza kuphunzitsa za kuipa kwa vutoli. Dziwaninso kuti achinyamata angathandize kuphunzitsa anthu onse osakhala achinyamata amnzawo okha.



Kuwunika momwe ntchito yayendera ndi kuchita kalondolondo



- Mfundo yofunika kuiunika bwino yosonyeza kuti zinthu zayenda bwino ndi mmene achinyamata atengera mbali komanso kupambana kwa zisudzozo ndiponso mmene zawakhudzira.
- Sungani mfundo zonse zimene mwalemba komanso kanema imene mwajambula popeza kuti izi zikhala zofunika pamaphunziro ena.
- Monga zinanenedwa nthawi ina, zisudzo ndi zothandiza kupereka mphamvu. Zimathandiza pa mmene achinyamata angakulire munjira zosiyanasiyana kuphatikiza pa kaganizidwe, komanso mmene akumvera pa za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu. Izi zingathandize kuthandiza pa nkondo yolimbana ndi mchitidwewu padziko lonse lapansi.
- Kudzera muzichitochito za msangulutso iwo angathe kufikira patali ndi uthenga wao.

Gawo ilila maphunziro ndi lolimbikitsa kuti ntchito yolimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu ikhale yoyang'ana ikupitilira patsogolo chifukwa ndi yosalilira zinthu zambiri, ndiponso makamaka imakhala ikupempha anthu kuti angachite kanthu.

Gawoli lomwe ndi loyesa kufanizira zimene zimachitika ndi lothandiza kuti munthu amvetse bwino za zisudzo zenizeni zazitali zokhala ndi mauthenga ochuluka. Izi ndi zothandiza anthu makamaka amene angafune kuti ayese kulemba sewero lenileni looneka kumaso kwa anthu.

Poonjezera apa palinso maphunziro ena amene angathandize kuti gulu lithe kumvetsa bwino za kukula kwa vuto la mchitidwe wogwiritsa ntchito ana. Izi zingatheke achinyamata atagwiritsa bwino ntchito zimene aphunzira pankhani ya mitsutso, kafukufuku ndiponso mmene mauthenga angapangiridwe ndi kufalitsidwa zimene zili m'magawo ena a maphunzirowa. Kuonjezera apo, palinso gawo lothandiza kutukula luso la kalembedwe ka zinthu za msangulutso.

Gawo Ioyamba la Zowonjezera

Masewero

Zisudzo Zolota Tanthauzo la Zizindikiro

Mtundu wa zisudzo uwu womwe sunawande kwenikweni m'maiko ambiri. Umakhala wothandiza kubweretsa mtima wofuna kupikisana ndipo wakhala ukugwiritsidwa ntchito pa masewero a pa kanema.

Monga mmene amakhalira masewero ena onse, zisudzo izi zili ndi malamulo ake ndipo amakhalanso osiyana malinga ndi dziko kapena dera limene munthu ali. Inu mukupemphedwa kutsatira zimene mukudziwa pa za zitsudzozi.

Pofuna kupereka chithunzi kwa ena amene sanaonepo kapena kumva za masewerowa, tapereka chithunzi chabe pansipa. Chofunika kuti mudziwe ndi choti masewerowa ndi ongofuna kuti anthu ena alote kapena kupeza okha mutu umene gulu likuonetsa.

- Gawani gulu m'timagulu tiwiri kapena titatu ndipo perekani manambala kwa timaguluto.
- Pemphani gulu lililonse kuti lilembe papepala mutu wa chimodzi mwa zinthu izi: nyimbo, buku, kanema kapena sewero.
- Apinde kapepalako ndi kulemba nambala ya gulu lawo papepalalo ndi kupereka kwa inu (wotsogolera maphunziro)
- Onse akapereka mapepala awo, ayikeni pamodzi muchina chake ngati chitini, mbiya kapena chisoti
- Kenaka pemphani munthu mmodzi kuchokera m'gulu lililonse kuti atolemo kamodzi

- Ngati angapezeke kuti atola kapepala ka gulu lawo lomwe mupempheni kuti abweze ndi kutola kena
- Gulu lililonse likhale palokha m'chipindamo, kapena m'zipinda zina ngati nkotheke
- Akuyenera kutengapo mphindi za pakati pa zitatu ndi zisanu kukonzekera kuti ayese kutchula mutu umene uli papepalapo popanda kulankhula koma pogwiritsa zizindikiro zokha
- Magulu enawo akuyenera kutanthauzira mutuwo polongosola
- Malamulo oyenera a masewerowa ndi awa:
- Ochita masewerowa asalankhule;
- Ochita masewero asayese kutchula zilembo ("**spelling**");
- Angathe kuonetsa kuchuluka kwa mau m'mutuwo;
- Angathe kusonyeza kuchuluka kwa maphatikizo a mawu ("**syllables**") kenako kuyesa kuchita zizindikiro zoimira maphatikizowo;
- Angathe kusonyeza kuti mutuwo ndi wa chiyani - nyimbo, kanema, bukhu kapena sewero kapena ndi wa phatikizo la zimenezi.

Zisudzo Zofanizira Anthu ndi Zinthu Zochitika 15

- Maguluwo akonzeke limodzi, poona mmene angagawanire ntchito ndipo akhale okonzeka kuchita masewerowa pamaso pagulu lonse.
- Cholinga cha gulu lonse ndi kuona kuti amene angathe kulota kapena kupeza mutu msanga kuposa ena ndi ndani.
- Ndi chachidziwikire kuti gulu lomwe linalemba mutuwo silitenga nawo mbali chifukwa iwo akudziwa kale
- Gulu lililonse lipatsidwe pakati pa mphindi imodzi ndi zitatu kuti zichite chisudzo chawo chosalankhulachi.
- Pamene maguluwa akugawikana kuti akakonzekere, inu muyese kuyenda ndi kukhala m'magulu osiyanasiyana ndi kuwathandiza mmene iwo angachitire poyerekeza kupereka zizindikiro za mau ena.

- Yesetsani kuti gulu lidziwe kuti zisudzo izi ndi zongofuna kuchita ngati mocheza ndithu zosati atayirepo mphamvu zao kwambiri.
- Dziwani kuti panthawi imene inu mukuzungulira m'magulu pamene iwo akukonzekera, ndibwino kuti muwakumbutse zanthawi yomwe yatsala.
- Ngati mwatsata bwino malangizo onse panthawi yokonzekera, zikuyenera kuti panthawi ino aliyense akhale akuona kuti ndi masewero osangalatsa zayenda bwino.

Zisudzo zosalankhulazingathe kukhala zachangu, zopangitsa achinyamata kuchita zinthu mofulumira ndi mozama ndiponso zosangalatsa. Zonsezi zingatheke ngati ndondomeko zonse zatsatidwa moyenera.

- Musalole kuti achinyamata alowe msanga ulesi kapena mphwayi.
- Alimbikitseni achinyamata kutenga mbali polongosola fundo kapena kufuula pa zimene akuganiza.
- Yesetsani kuti pakhale phokoso losonyeza kukondwa popeza kuti izi ndi zothandiza kuchotsa manyazi ndi kupangitsa achinyamata kuti amasuke.
- Bweretsani kamtima koti pakhale kupikisana, mwachitsanzo, mungathe kunena kuti gulu limene muli amenewalota bwino msanga za zizindikirozo ndi limene lachita bwino, osati munthu mmodzi yekhayo.
- Yesani kuchita nawo zolongosola kapena kulota zizindikirozo pofuula nawo.
- Chisudzo chimodzi chikatha, yesetsani kuti chinzake chibwere msanga m'bwalo kuti zonse zipitilire bwino.
- Nthawizina anthu amene akudziwa zisudzo zosalankhulazi bwino lomwe amanamizira kuti sakudziwa chilichonse ndi cholinga chofuna kuti masewerowa apatse mwayi wotengambali kwa amnzawo ndiponso kuti achitike kwanthawi yaitali. Iyi ndi mbali imodzi yopangitsa kuti masewerowa akhale osangalatsa.
- Zonsezi ndi gawo lomwe cholinga chake ndi kusangalatsa ndi kupatsa achinyamata chidwi choti athe kuchita zinthu.
- Perekani mwayi kwa gulu kuti lithe kuyendetsa zinthu mwandondomeko yoyenera. Inu musachite nawo zolota mitu ya zizindikiro.

- Komabenthawi zina ndi kofunika kuti inu muthandize pamene achinyamata akulephera kupereka yankho lokhoza pamutu umene zizindikiro zake zikuonetsedwa.

Zochitachita za Zisudzo (*Drama exercises*)

- Cholinga chachikulu cha zochitachita izi ndi kuyesa kupangitsa kuti achinyamata akhale omasuka pamalo pamene iwo akukumanira. Motero iwo amaphunzira mmene angakhalire momasukirana ndi amnzawo ndiponso amayesa kuchita zinthuzosiyanasiyana. Pochita izi, iwo amatha kulakwitsa komabe amakhala ndi chikhulupiliro mwa iwo okha.
- Mfundoiyi ndiyofunika kwambiri chifukwa kukhala wodzikhulupilira ndi chinthu choyamba chimene chingawapangitse kuti athe kuchita nawo zisudzo. Choncho, zambiri mwa zochitikazi zimakhala zoseketsa, zokoma ndipo pang'onopang'ono zimakhala zikuwatengera ku luso ndi bwalo lochita zisudzo.
- Uzani gulu lonse kuti cholinga cha zochitika zonsezi ndi kubweretsa chimwemwe ndipo zikufunika kuti iwo adzipereke kwathunthu pa zonsezi.
- Pali zochitachita mazanamazana zamsangulutso za zisudzo zimene zimagwiritsidwa ntchito pa maphunziro osiyanasiyana ndiponso ndi magulu a anthu a misinkhu yosiyanasiyana.
- Ngati mungakhale ndi mwayi wopeza zolembalemba zokhudza izi, yesetsani kutero chifukwa zimakhala zothandiza kwambiri paliponse pamene pali gulu la anthu. Zina mwa izo ndi masewero omwe nkutheka kuti achinyamata anazidziwa ali ocheperako misinkhu ndipo mwina iwo angakayike kuti achitenso masewero amtunduwu nthawi ino pamene akula, makamaka anyamata.
- Inu ntchito yanu ndi kuwalimbikitsa kuti athetse manyazi ndi makhalidwe aliwonse amene angakhale olepheretsa kuchita masewero a mtunduwu kuti azindikire kuti pokumbutsa zakale angathe kudabwa kuona kusangalatsa kwake.

Kuzungulira Mipando Potsata Nyimbo (*Musical chairs*)

- Malinga ndi kukula kwa gulu lanu, mukuyenera kuligawa m'timagulu tocheperako
- timagulu tocheperako
- Mukhale ndi chida choyimbira nyimbo za matepi kapena ma **CD**. Ngati

palibe, munthu wina angathe kumaimba chida chilichonse chimene gulu lingamamvetsere kapena kumaimba kuti iwo adzimva.

- Uzani gulu limodzi kuti likhale pamipando pakati pachipinda chimene inu muli. Iwo akhale m'mizere iwiri koma cholozana misana.
- Poika mipando muonesetse kuti umodzi uperewere poganizira kuchuluka kwa gululo.
- Nyimbo ikayamba kuimba, gulu lonse livine (poyenda kapena pothamanga) mozungulira mipandoyo.
- Pamene nyimboyo yasiya kuimba, aliyense apeze mpando woti akhale.
- Amene akhale wopanda mpando ndiye kuti watuluka m'masewerowa.
- Aliyense ayimilire ndipo mpando umodzi uchotsedwenso pamalopo pofuna kuonesetsa kuti umodzi uperewere poganizira anthu amene alipo m'gululo.
- Masewerowa apitilire mpaka patsale mmodzi yekha yemwe ndi wopambana paguleyu.

Kuvina ndi Kuyenda Potsata Nyimbo (*Musical statues*)

- Mukhale ndi choyimbira chogwiritsa matepi kapena ma **CD**.
- Gulu lonse likhale likuyendayenda kapena kuvina m'katikati mwabwalo la chipindacho pamene nyimbo ili mkati.
- Pamene nyimbo yaimitsidwa, aliyense ayime chilili pamalo pamene ali, kaya mwendo unali mmwamba, iye asasunthe.
- Wotsogolera maphunziro kapena wina aliyense wosankhidwa ayang'anitsitse pofuna kuona ngati wina wasuntha kapena kuyenda nyimbo itasiya kuimba.
- Aliyense akhale chilili, osaseka kapena kuphethira.

- Aliyense wopezeka akutero atulutsidwe m'masewerowa nthawi yomweyo.
- Masewero apitilire ndi nyimbo mpaka patsale m'modzi wotsala yemwe ndi wopambana.

Kuphana Maso ndi Maso (*Eye shoot*)

- Gulu lonse liime pochita bwalo lalikulu lozungulira.
- Ndikofunika kuti aliyense athe kumaona wina aliyense pabwalopo.
- Mmodzi asankhidwe kuti ayambitse masewerowa
- Cholinga chake ndi kuyesetsa kuti akumane maso ndi maso ndi diso la munthu wina aliyense pabwalopo.
- Posachotsa maso pa diso la munthuyo, iye ayende ndi kukakhala pamalo a munthuyo.
- Pamene winayo akupita kukakhala pamalo a munthuyo, amene wayang'anidwayo naye asankhemunthu mmodzi yemwe angamuyang'ane mosabweza maso.
- Panthawi yomwe wakomana maso ndi maso ndi winayo, ayambe kuyenda nthawi yomweyo kupita pamalo pakepo.
- Apa munthu wachitatuyo nayenso ayang'ane ndi kukumana maso ndi wina wachinayi ndipo ayambe kuyenda kupita pamalo pakepo.
- Wachinayi woyang'anidwayo naye ayang'ane mozungulira ndi kuphana maso ndi maso ndi munthu mmodzi ndikuyamba kuyenda nthawi yomweyo kukaima pamalo atsopano a mzakeyo.
- Zimene zimachitika ndi zoti anthu angapo amakhala akuyenda kuchoka malo ena kupita malo ena kudutsa pakati pabwalopo uku akumuyang'ana mmaso mwake.
- Muonetsetse kuti pasakhale kulankhula, ndipo wina asaseke (zimene ndi zovuta ndithu!).
- Masewerowa amakhala osangalatsa kwambiri ndipo amafunika kuti akhale akuchitika kwa kanthawi kakatali.

Masewero Okumbikira (*Memory game*)

- Gawani gululo pawiri.
- Gulu lililonse lipeze malo ake m'chipindamo.
- Mmodzi asankhidwe kukhala chiboliboli.
- Iye ayime chilili, mosasuntha ndipo wina ayende momuzungulira kuyesa kuonesetsa mmene iye wavalira kuti adzathe kukumbukira pambuyo pake.
- Apatsidwe mphindi imodzi yochita izi.
- Onse atseke maso kwa mphindi imodzi pamene mmodzi uja amene ali chiboliboli akuyesa kusintha zinthu zisanu ndi chimodzi kuti aoneke mosiyana. Angathe kuchita zinthu ngati izi: kuchotsa mphete, ndolo, kumasula batani kapena mabatani ena, kumasula chingwe cha nsapato, ndi zina zimene angathe kuchita.
- Pamene onse abwelera uja anamuonetsetsa munthu uja poyamba apatsidwe mphindi imodzi kuti ayese kuona zimene zasintha.
- Kenako asinthane ndipo achite monga zachitikira pamwambapa.

Dengu la Zipatso (*Fruit basket*)

- Anthu onse akhale pansi ndikupanga bwalo mozungulira ndipo ayang'ane mkati mwa bwalo.
- Onse adzitha kuonana.
- Patsani aliyense dzina la chipatso potsatira mmene imayendera mivi ya wotchi kapena mbali inayo ngati mwafuna kutero.
- Maina a zipatso oti aperekedwe alipo anayi: **apple**, lalanje, nthochi ndi peyala.
- Woyambayo akhala **apple**, wachiwiri lalanje, wachitatu nthochi ndipo wachinayi peyala.
- Wachisanu akhalanso **apple**, wotsatira lalanje, nthochi ndi peyala ndipo izi zipitilira mpaka aliyense akhale ndi dzina.

- Imani kunja kwa bwalo ndi kutchula dzina la chipaso chimodzi.
- Mukatero aliyense amene watenga dzina lachipatsocho athamange kupita kukakhala pa mpando wa wina wofanana naye dzina.
- Iwo angathe kuthamangira mbali iliyonse imene akufuna, koma ayenera kukhala pansi msanga.
- Pamene mukutchula dzina la chipatso chilichonse mudzikhala mutaima kumbuyo kwa mmodzi wa dzina limenelo, kenako kuchotsapo mpandowo mwini wake akangodzukapo.
- Izi zikusonyeza kuti nthawi zonse wina adziperewera malo okhala ndipo adzituluka masewerowo ndi kuima kunja kwa bwalo.
- Poonjezera pakutchula dzina lachipatso chimodzi, mungathenso kutchula "dengula zipatso" ndipo aliyense adzuka kukafuna mpando wina wokhala.
- Pasapezeke wokhala pansi panthawiyi ndipo onetsetsani kuti aliyense wakakhala pamalo ena.

Kutsatira Malangizo ndi Kuchita Zosiyanasiyana (*Point leggah*)

- Gulu lonse liyamba kuyenda molowera mbali iliyonse yachipinda chimene mGulu lonse liyamba kuyenda molowera mbali iliyonse yachipinda chimeneuli.
- Mphunzitsi kapena wina amene wasankhidwa kutsogolera masewerowa alamule mofuula: "Dumphani", "Lozani", "Khalani Pansi".
- Pamene wotsogolera akulamulira chonchi, onse atsatre zimene zikulamulidwa. Panthawiyi iwo adzibwereza kufuula zimene zalamulidwa.
- Wotsogolera ayambe kulamula zinthu zina zosiyanasiyana zovutirapo kuchita.
- Zinthu zimayamba kuchitika mofulumira kwambiri ndipo pamakhala phokoso lochuluka.
- Masewerowa amakhala bwino m'chipinda chachikulu, kapenanso panja pabwalo.
- Popeza masewerowa amakhala ofulumira ndipo opatsa phwete, achinyamata amakondwa nawo kwambiri.

- Sinthani munthu wolamulira pambuyo pa kanthawi kuti pabwere maganizo ena.

Pangani ... (*Make a ...*)

- Wotsogolera atchula maina azinthu zosiyanasiyana monga ngati mandala, tipoti (*tea pot*) kapena telefoni.
- Mamembala abwere pamodzi ndi kupezeka m'timagulu ta anthu asanu ndi kupanga chinthucho pogwiritsa ntchito matupi awo.
- Izi akuyenera kuchita mu theka la mphindi (30 **seconds**).
- Akangomaliza kupanga chinthu chimodzi, wotsogolera auze anthu ena onse kuti ayende ndi kuona zinthu zosiyanasiyana zimene zapangidwa ndi matupi a anthu.
- Kenako atchule chinthu china.

Nyimbo ya Maina (*Name chants*)

- Gawani gulu lonse m'timagulu tating'ono ta anthu anayi lililonse.
- Gulu lililonse lipatsidwe mphindi zisanu kuti lipeke nyimbo yaifupi kugwiritsa ntchito maina awo.
- Angathe kuimba mulimonse mmene akufunira, kaya ngati kwaya, kaya ngati zamakono zija amatchula *rap*.
- Kenako ayimbe nyimbo yawo ena onse akumvera.

Kuponya Maina (*Name throwing*)

- Onse ayime popanga bwalo lozungilira.
- Ngati gulu lanu ndi lalikulu kwambiri, mungathe kuligawa kuti lililonse likhale ndi anthu asanu ndi mmodzi (6).
- Maguluwo aziponya mpira kupita ku magulu ena.
- Poponya mpirawo, amene ali m'gulu limene mpirawo waponyedwera atchule dzina la munthu amene waponya mpirawo.

- Ukaponyedwa ku gulu lina, wina wagulu limene mpirawo wapita atchulenso dzina la woponyayo pamodzi ndi ena onse amene anaponya mpirawo poyamba mpaka woyamba weniweni.
- Masewerowa angathe kusinthidwa kuti mwina adzitha kulongosola mmene woponyayo akuonekera pogwiritsa ntchito liu limodzi, awiri kapena atatu.
- Mwinanso angathe kumatchula dzina la woponyeredwa mpirawo.

Bwalo la Maina ndi Zakudya (*Names and meal circle*)

- Uzani onse kuti apange bwalo lozungulira koma mbali imodzi yabwalo ikhale yotsegula kuti onse azitha kuonana.
- Kuyambira kumanzere, aliyense atchule dzina lake ndi chakudya chimene machikonda kwambiri momveka bwino.
- Akangomaliza kutchula, mnzake amene ali pafupi abwereze zimene iye wanena ndipo iye mwini atchule dzina ndi chakudya chimene amachikonda.
- Aliyense akumbukire chakudya cha amnzake onse amene atchula pambuyo pake, kenako kutchula dzina lake ndi chakudya chake.

Mizukwa (*Vampires*)

- Mamembala a gulu lonse ayende mozungulira m'chipinda atatseka maso.
- Pamene akuyenda akhudzidwa m'musi mwa nkongo yawo ndi m'modzi amene wasankhidwa kukhala "mzukwa".
- Aliyense wokhudzidwa agwa ndi kunamizira kufa uku akufuula kwambiri mwamantha.
- Zikatero, iwo adzuka ndi kusanduka "mzukwa" ndipo anka nafuna anthu oti *awalume*.
- Mzukwa ukaluma mzukwa wina, onse asandukanso anthu uku akufuula ndi chimwemwe maso ali chitsinzinire.

Makina Ofanizira Zinthu (*Mime machines*)

- Munthu m'modzi asankhidwe ndi kuima pakati pabwalo limene lapangidwa.
- Auzidwe kuti alire ngati makina ena aliwonse amene angayerekeze.
- Wotsogolera auze ena kuti alowe nawo m'bwalo ndikumapitiriza phokoso la “makinawo” koma kulira kwake kukhale kofanana ndipo asaleke kulira.
- Amene alowa nawo m'bwalo angathe kuyesa kupangitsa kuti makinawo alire mofulumira kapena mochedwerako mpaka atafika poti makinawo ayima kapena kusiya kulira.
- Izi zikamachitika, onse azililira limodzi.

Namlondola (*Colombian hypnotism*)

- Anthu akhale awiri-awiri
- M'modzi atsatire dzanja lotsegula la mnzake koma osalikhudza.
- Ayesetse kuti asasinthe mbali imene akutsatira, ngati kuli cha kumanja kukhale kumanja komweko, kaya kumanzerezikhaleenso chimodzimodzi.
- Ikafika nthawi ina asinthane ndipo achitenso chimodzimodzi.

Kupuma Limodzi (*Breathing together*)

- Gulu lipange bwalo lozongulira kuti onse adzitha kuonana.
- Popanda kulankhulana, ayesetse kuyamba kupuma mofanana.
- Pasapezeke wina wofulumira kapena kuchedwa.

Kufanizira ndi Kutanthauzira Zochitika (*Tableaux - moving tableaux*)

- Gawani gulu lanu m'timagulu tocheperako kapenanso anthu angathe kukhala awiri-awiri.
- Theka la gululo lipange kapena lionetse chithunzi cha mmene mwana angagwiritsidwe ntchito yoposa msinkhu wake, kapena zotsatira zake mopanda kusintha.

- Theka linalo liyang'anizane ndi loyambalo ndi kukhala ngati kalilole (**mirror**) pobwereza zimene gulu loyambalo likuchita.
- Gulu loyamba lija liyamba kuyenda pang'onopang'ono kukhala ngati akutsatira chithunzi chimene chapangika pagalasi chija.
- Nalo gulu linalo lichitenso chimodzimodzi, kutsatira zimene gulu loyambalo likuchita.
- Amene akuonelera ayese kufunsana ngati matanthauzo amene iwo apeza ali ofanana ndipo akambirane zimene magulu awiriwo amatanthauza.

Kulongosola Zochitika (*Story to script*)

- Anthu akhale awiri-awiri
- Woyamba wotchedwa **A** auze wachiwiri, yemwe tingamutchule **B**, nkhani ya ziganizo zitatu yokhudza mwana amene akugwira ntchito.
- Nkhaniyo ikhale ndi poyambira, pakati pake ndiponso pothera.
- **B** amvere mwachidwi zimene **A** akunena ndipo aonjezere afotokozi (*adjectives*) ngati nkotheke.
- **A** auzenso **B** nkhaniyo kugwiritsanso ntchito afotokozi amene **B** anagwiritsa ntchito ndipo iye aonjezerepo mau olongosola mmene zinthu zikuchitikira (ma adiverebu)
- Apitirize kuuzana nkhaniyo poonjezeramo maphokoso kapena zizindikiro zamanja zina zosiyanasiyana, kupotoza nkhope mwanjira iliyonse komanso kudzigwedeza mmene akufunira.
- Potsiriza ayimilira ndikusandutsa nkhani yawo ngati sewero, wina akuchita zizindikiro wina akulongosola, kapena onse akuchita limodzi ngati zisudzo zokhala ndi anthu awiri.



Lekani Kugwiritisa Ntchito Ana

ILO
International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0- 1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipec

ISBN 92-2-113240-4

